# NTCHEU DISTRICT EXAMINATION BOARD

## 2023 PSLCE DISTRICT MOCK EXAMINATION

## CHICHEWA

**(Malikisi 100)**

**Subject Number: P**

**Time Allowed: 2hrs 15min**

**1:30 – 3:45pm**

**Dzina lanu:** ______________________________________________ (Surname First)

**Dzina la sukulu yanu:** ______________________________________________

**Malangizo**

1. **Onetsetani kuti pepalali lili ndi masamba asanu ndi atatu.**
2. Lembani dzina lanu ndi dzina la sukulu yanu m'mipata yomwe yaperekedwa
3. Pepalali lili ndi magawo anayi, Gawo **A**, **B**, **C** ndi **D**.
4. Yankhani funso limodzi mu Gawo **A**, ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo **B**, **C** ndi **D**.
5. Zungulizani lembo lomwe lili ndi yankho lokhoza mu Gawo **D**.
6. Mutebulo lomwe lili pa tsamba lino, chongani nambala la funso lomwe mwayankha.
7. Perekani pepalali nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani ngati mwayankha | Musalembe muno | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

**Turn Over**

**GAWO A** (Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere **100** koma asabzole 150

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu"MUDZI WATHU" polemba tsatirani izi.

**Ndime yoyamba**

- Dzina la mudzi wanu.
- Chigawo cha boma lomwe mudziwo umapezeka.

**Ndime yachiwiri**

- Ena mwa magule omwe anthu a mmudzimo amavina.
- Zina mwa mbewu zomwe anthu amalima ndi ziweto zomwe amaweta mmudzimo.
- Zina mwa njira zomwe anthu amapezera chuma.

**Ndime yachitatu**

- Ena mwa mavuto omwe anthu a mmudzimo akukumana nawo ndi momwe angathetsere mavutowo.
- Mungatani mutaona munthu akuononga za chilengedwe

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa agogo anu yowadziwitsa kuti mudzapita kukawachezera patchuthi mukalemba mayeso anu a Sitandade 8. Mwa zina tsatirani izi polemba.

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata yanu.
- Tsiku lomwe mudzapite kwa agogo anuko.
- Nthawi yomwe mukakhale kutchuthiko.

**Ndime yachiwiri**

- Yemwe mudzapite naye kutchuthiko.
- Zomwe mudzatenge popita kutchuthiko.
- Chisangalalo chomwe mudzakhale nacho mukadzapita kutchuthiko.

**Ndime yachitatu**

- Zomwe mukuyembekezera kudzachita kutchuthiko.

___

___

___

___

___

___

___

## GAWO B (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

Pamudzi pa a Mwadzaangati kudali mtsikana wina dzina lake Ndaonazino. Agogo ake a Nanthochi ndiwo adamupatsa dzinali. Iyeyu adali mtsikana mmodzi yekha mwa ophunzira m'mudzimo amene adafika ku Sekondale. Mtsikanayu adali chitsitsamsepe cha bambo ndi mayi Tidyenawo.
M'mudzi mwawomo, makhumutcha adali owerengeka kotero ambiri adali a kapunthabuye. Ambiri amadya zogagada ndi nkhwangwa ndipo amagona palumbe. Ngati njira imodzi yopezera ndalama Ndaonazino akakhala patchuthi amapezeka pamalo okwerera basi pomwe amachitapo malonda. Pamalopa pamamveka kuti, "Tipeze mazira ophika pamtengo waukazi wa K50 yokha basi, amboba, masiteni, magaye komanso mafana nonse osafinyika."
Ndaonazino amachokera m'banja lomwe linali lotakataka. Ngakhale kuti Ndaonazino ankagulitsa malonda ake pamalo okwerera basi, iye nthawi zonse amaganda makande popita ndi pobwerera kwawo. Nthawi zonse makolo a Ndaonazino amamulangiza kuti sikadza kokha kamaopa kulaula choncho amamulimbikitsa pamalondawo komanso amati akabwera kutchuthi amamupatsa tindalama toyambira bizinezi. Ndaona zino amapikula nzimbe, ndiwo zamasamba kapena malonda aliwonse omwe amadziwa kuti akhonza kum'kankha. Akatero amathandiza makolo ake kulipira ndalama za maphunziro ake.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa.

a. Kodi makolo a Ndaonazino adali yani?
_______________________________________________ (Malikisi 1)

b. Tchulani amene anamupatsa dzina loti Ndaonazino?
_______________________________________________(Malikisi 1)

c. Kodi Ndaonazino adali mwana wachingati m'banja mwawo?
_______________________________________________
(Malikisi 1)

d. N'chifukwa chiyani Ndaonazino amapezeka pamalo okwerera basi?
_______________________________________________(Malikisi 1)

e. Perekani zining'a kuchokera m'nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:
   i. Kupeza zinthu movutika_______________________________________________
   ii. Kugona osafunda_______________________________________________
(Malikisi 4)

f. Perekani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi m'nkhaniyi:
   i. Ganda makande _______________________________________________
   ii.Sikadza kokha kamaopa kulaula _______________________________________________
(Malikisi 4)

g. Kodi Ndaonazino amathandiza bwanji makolo ake?
_______________________________________________ (Malikisi 1)

h. Forokozani zomwe zikutsimikiza kuti Ndaonazino adali wosamala ndalama zomwe ankapeza?
_______________________________________________ (Malikisi 2)

i. Kupatula kugulitsa nzimbe, ndi malonda ena ati omwe Ndaonazino amagulitsa?
_______________________________________________
(Malikisi 1)

j. Kuchokera m'nkhani mwawerengayi, konzani mawu otsatirawa m'chichewa choyenera:
   i. Amboba_______________________________________________ (Malikisi 1)
   ii. Mafana _______________________________________________(Malikisi 1)

k. Fotokozani zomwe zikutsimikiza kuti mudzi wa Mwadzangati udali wotsalira pachitukuko?

______________________________________________________________

______________________________________________________________ (Malikisi 2)

**GAWO C. (Malikisi 10)**

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. a. Werengani kankhanika ndipo yankhani mafunso otsatirawa.

"Ndizomvetsa chisoni ndithu kuti bamabo Chimtengo agona ulendo wosabwerera. Adali munthu wofunikira kwambiri m'mudzi mwanga."

**Mafunso**

i. Ndi malonje anji aperekedwa mkankhanika?

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

ii. Akulankhula malonjewa ndi ndani?

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

iii. Kodi mawu oti "agona" akutanthauzanji m'nkhaniyi?

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

b. Tchulani njira zodzitetezera ku matenda a Kolera.

______________________________________________________________(Malikisi 2)

5. Kupanga ziganizo

Lembani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. "nyalanyaza"

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

b. "khundabwi"

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

c. "sinza"

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

d. "ndwii"

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

e. "namwino"

______________________________________________________________ (Malikisi 1)

**GAWO D (Malikisi 40)**

Zungulizani lembo losonyeza yankho lokhoza (**A, B, C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa.

Mafunso 6 mpaka 10. Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

6. <u>Chisomo</u> wapha nkhuku.

A. Mneni C. Mvekero

B. Dzina D. Mlowammalo

7. Adammenya ndi <u>ichi</u>.

A. Mlowammalo C. Dzina

B. Mfotokozi D. Muonjezi

8. Adabwera pa galimoto.
A. Mneni C. Muonjezi
B. Mlumikizi D. Mperekezi

9. Mukamutenge osati mukammenye.
A. Mfotokozi C. Mlumikizi
B. Mperekezi D. Muonjezi

10. Ali pachikondi cha ndii.
A. Mvekero C. Mfuwu
B. Mneni D. Mperekezi

Mafunso 11 mpaka 15: Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

11. Yohane akusewera mpira
A. Mwininkhani C. Pamntherankhani
B. Mtsirizo wa mneni D. wa malo

12. Zuze, Katakwe wadwala.
A. Mwininkhani C. Mwininkhani
B. Pamtherankhani D. Dzina lapadera

13. Kumudzi kwathu kulibe ufiti.
A. Wa malo C. Mwininkhani
B. Pamtherankhani D. Mtsirizo wa mneni

14. Fisi wagwira mbuzi
A. Loyitanira C. Mwininkhani
B. Mtsirizo wa mneni D. Pamntherankhani

15. Chimwemwe bwera kuno.
A. Pamntherankhani C. Loyitanira
B. Mwininkhani D. Mtsirizo wa mneni

Mafunso 16 mpaka 20: Sankhani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

16. Maliya masula chingwecho.
A. tenga C. tola
B. khwefula D. manga

17. Kale anthu ankavala zikopa
A. Makono C. Tsopano
B. Make dzana D. Pano

18. Mpeni uwu ndiwobuntha.
A. wogontha C. wocheka
B. wakuthwa D. woipa

19. Madalitso walephera mayeso.
A. wakwanitsa C. wapambana
B. walakwa D. wazemba

20. Mulungu dalitsani Malawi.
A. khaulitsani C. wonjezerani
B. lemekezani D. tembelerani

Mafunso 21 mpaka 25: Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.

21. Kulamula vumbwe nkulinga uli ndi nkhuku.
A. Mnzako akavutika mthandize
B. Kupalamula milandu nkulinga uli ndi podalira.
C. Nkhuku imaphedwa pamilandu.
D. Wosauka sapalamula.

22. Kukana nsalu ya akulu n'kuviika
A. Kulola kuchita chinthu chifukwa cha manyazi akulu akakutuma
B. Ntchito imakoma ndi kuthandizana
C. Osayankhula nkhani yomwe sunayimvetsetse
D. Kukana kulandira chinthu chomwe sichako.

23. Khoswe wapatsindwi anaulula wa padzala.
A. Mavuto wawona mnzako atha kubwera kwa iwe.
B. Ukaputa mulandu usathawire kwa mnzako.
C. Mwayi umabwera pa mwayi wina.
D. Nkhani imawulula inzake yakale yobisika.

24. Awonenji adapha mvuwu mmono.
A. Khama lipindula
B. Munthu amene amaoneka onyozeka amachita zinthu zazikulu nthawi zina.
C. Ukasangalala kwambiri tsoka silichedwa kukupeza.

D. Munthu wamkulu umatha kuphedwa ndi mwana.

25. Walira mvula walira matope.
A. Ukafuna kupeza zabwino konzekera kukumana ndi mavuto.
B. Mvula imabweretsa matope.
C. Zabwino zili mtsogolo.
D. Chisoni umalira nacho.

Mafunso 26 mpaka 30. Sankhani mitundu ya msintho ya aneni omwe atsekedwa mnzere kunsi kwao.

26. Kodi ndi zoona kuti akwatirana.
A. wochitidwa C. wochitirana
B. wochititsitsa D. wochitira

27. Buku lija lapezeka
A. wochitidwa C. wochitirana
B. wochititsitsa D. wochitidwa poyera

28. Iye wamangitsitsa thumba lake
A. wochitirana C. wochititsitsa
B. wochititsa D. wotsutsa

29. Natchereza amagonagona m'kalasi.
A. wochititsa C. wochitirana
B. wobwerezabwereza D. wochitsitsa

30. Iye wamenywa.
A. Wochitira C. wochitirana
B. wonyazitsa D. wochititsitsa

Mafunso 31 mpaka 35: Sankhani mitundu ya awonjezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

31. Bambo Phiri apita kumunda.
A. wamuyeso C. wamchitidwe
B. wamalo D. wanthawi

32. Ukufuna ukhale pati?
A. wamalo C. wanthawi
B. wamuyeso D. wofunsa

33. Amalankhula molalata
A. wamakhalidwe. C. wamalo
B. wamaonekedwe. D. wamuyeso

34. Bwerani kuno kuti mudzadye.
A. wanthawi. C. wamaonekedwe
B. wamakhalidwe D. wamalo

35. Mwanayo wamenyedwa kwambiri.
A. wamuyeso C. wamchitidwe
B. wacholinga D. wamaonekedwe

Mafunso 36 mpaka 40: Sankhani magulu a maina omwe ali mmunsimu

36. Tolombolombo.
A. U ___ Ma C. Chi ___Zi
B. Mu ___A D. Ka___ti

37. Nsomba
A. Chi___Zi C. Ku__Pa ___Mu
B. LI ___Ma D. I ___Zi

38. Kumunda
A. Ku ___Pa ___Mu C. Mu ___ A
B. Mu ___Mi D. U ___ Ma

39. Mkate
A. I ___ Zi C. Mu ___ Mi
B. Li ___ Ma D. U ___ Ma

40. Chigoli,
A. I ___ Zi C. Li ___ Ma
B. Chi ___Zi D. Ku ___Pa___Mu

Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani mitundu ya nthambi za chiganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo.

41. Chimene akufuna sanandiuze.
A. Yadzina C. Yamfotokozi
B. Yamuonjezi D. yoyima payokha

42. Chuma chimene wabacho ufa nacho.
A. Yamuonjezi C. Ya mfotokozi
B. Ya dzina D. Ya muonjezi

43. Ndidzabwera ndikadzamaliza mayeso.
A. Yadzina C. Yamfotokozi
B. Yoyima payokha D. Ya muonjezi

44. Agogo anafuula pamene anaona njoka.
A. Yamuonjezi C. Ya dzina
B. Yoyima payokha D. Yamfotokozi

45. Adalanda mabuku omwe tidaba ku Zomba.

A. Yamfotokozi
B. Yamuonjezi.
C. Yoyima payokha
D. Ya dzina

**MAFUNSO ATHERA APA.**